# MALAMULO MALEMBA NDI MAWERUZIRO

Kalendala
ya Pangano
la Yahuwah

*Kugawa Moyenera Mawu A Choonadi*

*Chondel:* **Dziwani** kuti timagwiritsa ntchito Dzina lenileni la Mulengi atate wathu wa kumwamba chifukwa muli Mphanvu mu Dzina lake. Ndipo dzina limeneri ndi YAHUWAH/YAHUAH chifukwa ili ndi dzina lenileni atate wathu, ndipo timagwiritsatso dzina lakuti YAHUSHA m'malo mwa Ambuye kapena Yesu.Dzina lakuti Yesu lilibe tanthauzo komanso ndikumasulira kolakwika,kuphatikiza apo ndi dzina lamwano kwambiri lonyoza mwana wa nkhosa wa weniweniYAHUWAH.

YAHUSHA amatathauza kuti YAHUWAH ndi opulumutsa ndipo palibenso wina. Yahu ndi chidule cha YAhuah Sha muchiheberi amatanthauza chipulumutso/kupulmusa chocho dzina la mwana wa Mlengi watenga dzina la Aatate wake ndi ntchito yomwe anampats kuti achite kwa mtundu wa anthu YAHU-SHA

YAHUWAH akuitanira tonse kuti tiyambe kuitanira padzina lake komanso la mwana wake osati maina olakwika komanso abodza monga yesu,mulungu,ambuye,yehova,Yahweh,ndi ena ambiri.

Mavesi onse a m'Baibulo atengedwa mu baibulo lotchedwa "Scripture Translation 2009," kupatulapo ngati tasonyeza Baibulo lina!

Malangizo a Yahuwah kwa anthu Ake nthawi zambiri amafotokodzedwa mwachidule pansi pa magulu atatu akuluakulu omwe ndi Malamulo, Malemba ndi maweruzo.

Zonse ndi zomanga ndi zamuyaya.

Ngati titathyola chimodzi mwa izo, tachimwa ndipo timakhala kuti tampandukira Yahuwah. Malamulowa alipo kuti atitetedze ndi kutipatsa moyo wabwino kuti atipatse moyo wodala komanso kutiteteza ku zoopsa, zowawa ndi mavuto.Tiyeni tiwerenge kuchokera pa ***NEHEMIYA 9:13-14,26-27***.

## MALAMULO, MALEMBA, MALAMULO AZINSEMBE NDI MAWERUZO,

## ZIKUSIYANA MOTANII?

### Kodi ntchito yonse ya munthu ndi yotani?

Tikuyenera kuopa (kulemekeza) Yahuwah ndikusunga Malamulo Ake chifukwa ichi ndi ntchito yonse ya munthu.

Mlaliki 12:13. Levitiko 18:4-5 'Chitani maweruzo anga, ndi kusunga malamulo anga, ndi kuyendamo. Ine ndine YAHUWAH wanu. 5 'Ndipo muzisunga malamulo anga ndi maweruzo anga, (Malamulo anga, malemba ndi maweruzo anga) amene munthu akawachita azakhala nawo ndi moyo. Ine ndine Yahuwah.

Kumbukilani chilamulo cha Mose mtumiki wanga, chimene ndinamuuza m'Horebe, cha kwa Aisrayeli onse, ndi malemba ndi maweruzo. Malaki 4:4 (KJV) Mosiyana ndi zimene Chikristu chimaphunzitsa, lamulo la Yahuwah silinathe "kuchotsedwa," kapena "kukhomeredwa pamtanda" kapena kuthetsedwa. Lamulo la Yahuwah likugwirabe ntchitompakana pano ndiponso YAHUSHA adzabwera adzalipedza likugwirabe ntchito kwa inu lero, taonani **Mateyu 5:17**. "Koma iye amene ayang'ana m'lamulo langwiro laufulu, nakhalabe m'menemo, wosati wakumva mkuiŵala, komatu wakuchita ntchitoyo, ameneyo adzakhala wodala m'zimene azichita" (Yakobo 1:25).

Pamene Yahuwah anasakha ana aIsraeli kukhala mtundu motsogozedwa ndi IYE kupyorela mu utsogoleri wa Mose, analamula dongosolo loyang'anira lomwe limathandizira kukhala mu njira yachilungamo (Duteronome 1: 16-17). Oweruza amenewa anayenera kuchita ntchito zawo zopatsidwa mogwirizana

ndi malamulo, malemba, ndi maweruzo amene Yahuwah adawalamulira mwachindunji (monga ndi Malamulo Khumi) kapena kudzera mwa amithenga Ake.

Tikaphatikiza pamodzi, malamulo, malemba ndi maweruzo a Yahuwah zimayala maziko olimba amoyo olungama ndipo njira zake ndizofunika kuyendetsera miyoyo yanthu. Zonse zili ndi mfundo zomwe zimagwira ntchito kwa anthu onse ndipo ndi zazikulu zokwanira kuti zigwirizane ndi zochitika zatsopano.

## GAWO1: LA MALAMULO

### *Malamulo khumi a Yahuwah*

Ndipo YAHUWAH ananena mau awa onse, nati:

***# 1 Ine ndine Yahuwah WAKO, amene ndinakutulutsa m'dziko la Aigupto, m'nyumba yaukapolo. Usakhale nayo milungu ina koma INE NDEKHA. (kusatsata chipembedzo ndi miyambo yachikunja).***

***# 2 Usadzipangire iwe wekha chifaniziro chosema, kapena chifaniziro chiri chonse cha zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko; kapena kuzitumikira;pakuti Ine Yahuwah wanu ndine Wansanje Wamphamvuzonse, wolanga ana chifukwa cha atate kufikira***

*mbadwo wachitatu ndi wachinayi wa iwo akundida INE; Ndikuchitira chifundo zikwi za iwo amene amandikonda INE, ndi kusunga Malamulo ANGA.*

*# 3 Musatchule (Musatenge) DZINA la Yahuwah wanu pachabe; pakuti Yahuwah sadzamuyesa wosachimwa amene atchula DZINA LAKE pachabe.*

*# 4 Muzikumbukira tsiku la Sabata, kuti likhale lopatulika.Masiku asanu ndi limodzi muzigwira ntchito, ndi kuchita ntchito zako zonse: koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yahuwah wako; kapena ng'ombe zanu, kapena mlendo ali m'nyumba zanu mwanu; Yahuwah anadalitsa tsiku la Sabata, nalipatula.*

*# 5 Lemekeza atate wako ndi amako: kuti masiku ako achuluke m'dziko limene Yahuwah wako akupatsa iwe.*

*# 6 Usaphe.*

*# 7 Usachite chigololo.*

*# 8 Usabe.*

*# 9 Usachitire umboni wonama mnzako.*

*# 10 Usasirire nyumba ya mnzako, usasirire mkazi wa mnzako, kapena wantchito wake wamwamuna, kapena wantchito wake*

***wamkazi, kapena ng'ombe yake, kapena bulu wake, kapena kanthu kalikonse ka mnzako.***

### *Kodi Mawu Akuti Malamulo Amatathauza Chani?*

Malamulo amatanthauza kusonkhanitsidwa kwa mfundo zimene zimakhazikitsidwa ndikuvomeredzedwa mwaufulu,zimene zimayenera kutsatidwa komanso kugwiritsidwa ntchito nthawi zonse.

Malamulo a Yahuwah ali ndi nthaŵi zoikidwiratu, monga ngati mapwando opatulika, kulongosola miyambo yofunika ngakhalenso kukhazikitsa njira zoyendetsera nkhani zina zofunika. Chifukwa chakuti zimaulula nzeru za Yahuwah zopulumutsira munthu ndi kusonyeza zimene Iye anaika patsogolo panthu.Malamulowa amalangiza kwambiri za makhalidwe olungama. Malemba onse ndi ofanana kuyambira GENESIS 1:1 mpakana CHIVUMBULUTSO 22:21"

...Mwachitsanzo,YAHUSHA pa mateyu 22:34-40 iye atafunsidwa za lamulo lalikuru iye anati,uzikonda YAHUWAH mlengi wako ndi mtima wako onse ndi moyo wako onse ndi mzeru zako zonse.Ili ndi lamulo lalikulu ndi loyamba.Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndi ili ,uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini,pa malamulo awiri awa mpokolowekapo chilamulo chonse ndi

aneneri.Chikondi ndi chimene chasunga moyo wonse wa munthu wagwiro ndi wolungama,chifukwa chimatithandiza kuti tisachimwire YAHUWAH ngakhalenso munthu zanthu pa dziko lino lapansi.Mtchimo lili lonse limene anthu timachita kumakhala kupanda chikondi pa zimene  Yahuwah adatilamulira komanso pa anzathu.Yahuwa watipatsa  malamulo ambiri kuti anthu ake tidzichita kuonetsera kumvera kwathu komanso chikondi chathu kwa iye,chonde tiyeni tiwerenge mavesi ali m'munsiwa chifukwa akuonetsa m'mene inu ndi ine tingaonetsere chikondi chathu pakumvera. Levitiko 11:2-47 BL92–

*Awa ndi ena mwa Malamulo, omwe amapezeka mu Torah:*

***Chakhumi ndi zopereka (Lev 27:30-31; Lev 27:17-18: Deut 4:5-6; Deut. 4:12-14; (Deuteronomo 4:40)***

***Kudya Mafuta a nyama (Lev 3:17; Levi 7:232-24)***

***Kudya magazi a nyama (Levi 3:17; Levi 7:26-27; Lev 17:13- 14; (Levitiko 19:26) Kuyang'ana umaliseche ndi zolaula (Lev 18:6-19; Lev 20:19-21)***

***Kugwiririra (Lev 219:20)***

***Kugonana ndi wachibale (Lev 20:10-12; Lev 20:13-17)***

***Kuchita dama (Lev 18:20; Lev 19:20)***

*Kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha (Lev 18:22; Lev 20:13-17)*

*Kugonana ndi nyama (Lev 18:23-24; Lev 20:13-17)*

*Osapereka malipiro anthawi yake komanso oyenera (Lev 19:13; Lev 19:15)*

*Kukhala wodzikonda kwa osauka (Lev 19:9-10; Lev 19:15; Lev 25:35-37)*

*Kunyoza kapena kuseka anthu olumala (Lev 19:14)*

*Kunyoza kapena kuseka okalamba (Lev 19:32)*

*Kukana alendo (Lev 19:33-34) Miseche (Lev 19:16)*

*Kusunga chakukhosi ndi kubwezera (Lev 19:17-18)*

*Kudulira ndevu kapena kumeta mbalimbali mwatsitsi lanu (Lev 19:27)*

*Kudula zipsera kapena zojambulajambula pakhungu lanu (Lev 19:28)*

*Kugulitsa mwana wako wamkazi kuti achite uhule (Lev 19:29) Kuyesa kulankhula ndi akufa (Lev 19:30; Lev 20:6)*

*Kuchita malonda mopanda chilungamo (Lev 19:35-37)*

*Kunyalanyaza Sabata la mlungu ndi mlungu (Lev 23:1-3) Levitiko 23:1-2*

## *GAWO2: MALEMBA*

### *Nyengo Zoikika Za Yahuwah*

Ndipo Yahuwah ananena ndi Mose, kuti, "Lankhula ndi ana a Isiraeli, ndipo uwauze kuti, 'Nthaŵi zoikidwiratu za Yahuwah zimene muzilalikira misonkhano yopatulika, nthawi zanga zoikidwiratu ndi izi:

Levitiko 23:1-44

- Sabata
- Paskha/Mkate wopanda chotupisa kwa masiku asanu ndi awiri
- Phwando la Zipatso Zoyamba
- Phwando la Masabata( Petekositi)
- Phwando la Malipenga
- Tsiku la Chitetezo
- Phwando la Misasa

# GAWO 3. MAWERUZO

## *Malamulo apachikhalidwe Levitiko 18*

Levitiko 26 Madalitso a Kumvera / Chilango cha Kusamvera

Levitiko 27 Malamulo Okhudza Malonjezo Ziweruzo za Yahuwah zimasonyeza mmene zosankha zolungama ziyenera kupangidwira mogwirizana ndi mfundo zovumbulidwa m'malamulo Ake. Amalangiza oweruza onse omwe ali ndi udindo woweruza kuti aweruze zofotokozedwa mwachindunji m'Torah: "Potsutsana iwo adziyima monga oweruza ndi kuwaweruza monga mwa Ziweruzo Zanga.

Iwo azisunga malamulo anga ndi malemba anga (Ezekieli 44:24) Yahuwah nawonso akuwauza kuti: "Musamaweruze mopanda chilungamo; Usamakondere wosauka, kapena kulemekeza munthu wamphamvu. Uziweruza mnzako m'chilungamo" (Levitiko 19:15). Potsatira ziweruzo za Yahuwah, osalakwa samatsutsidwa ndipo olakwa ali ndi udindo wobwezera zoyenera zoperekedwa kwa wolakwilidwayo.

Lingakhale dziko ndilodabwitsa kwambiri chifukwa lili ndi Malamulo ambiri amene sapangae dziko lino kukhala malo abwino koma amateteza anthu oipa m'dzikoli ndipo chilungamo chenicheni sichimachitidwa kwa osalakwa. Pali kusiyana

koonekeratu pakati pa lamulo (lamulo kapena lamulo loyenera kutsatiridwa ndi kusungidwa) ndi chiweruzo (njira yochitira zinthu pakati pa anthu Ake). Zonsezo ndi zofunika koma zomvetsa chisoni chifukwa tadalira munthu ndipo tataya tanthauzo lenileni la chilungamo ndi chikondi kwa anthu anzathu.Ngati sitimvera malamulo, ndi ziweruzo  zidzatichitikira pa tsiku la chiweruzo. Yahusha atatikana ndikutiponya kunja.Machimo ena amene timasankha kupitiriza kuchita chifukwa timawakonda adzatiikira pa tsiku la chiweruzo ndipo tidzataya moyo wathu wosatha. Yahuwah sanyozedwa. Iye amafuna kuti tizimumvera kotheratu osati chifukwa cha mantha, koma chifukwa chakuti timamukonda komanso kumvetsa zimene uchimo wachita padzikoli. Ndi zoipa kwambiri ndipo anthu osalakwa akuvutika tsiku ndi tsiku AGALATIYA 6:7.

Yahusha wakaamba kuti: "Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha koma ndimau onse utuluka mkamwa mwa Yahuwah Mateyu 4:4 Ngati muwerenga buku lonse la Malaki 4 muwona kuti mutuwu ukunena za chiwonongeko cha nthawi yakumapeto kwa dziko lapansi ndipo zisanachitike kuti YAHUWAH anenanso kuti KUKUMBUKIRANI chilamulo cha Mose mtumiki wanga,chimene ndinamulamulira m'Horebu kuti chikhale chaa Israyeli yense; ndi malemba ndi maweruzo. Malaki 4;4.

N’chifukwa chiyani Yahuwah anaika zimenezi mu ulosi wa nthawi yotsiriza n’kunena kuti atangotsala pang’ono kuti uthenga wa Eliya ulalikidwe, tiyenera kukumbukira malamulo ake ndi ziweruzo zake zomwe zikuphatikizapo madyerero a Yahuwah.

Panali nthawi zonse nsembe za nyama pamasiku a madyerero a Yahuwah koma panalinso nsembe za nyama zowirikiza kaŵiri pa Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Ndiye zitheka bwanji kuti anthu azisunga Sabata popanda kufunikira kopereka nsembe za nyama koma sadzakondwerera masiku a Phwando la Yahuwah la Pachaka koma kuti apitirire mu maholide achikunja monga Khrisimasi, Isitala, tsiku la Valentine, tsiku la Amayi ndi zina zambiri.

Yahusha ndi “Mwanawankhosa” wathu wangwiro amene anaperekedwa nsembe chifukwa cha machimo athu choncho unsembe wa Alevi, miyambo ya m’kachisi ndi nsembe za nyama sizikufunikanso chifukwa nsembe ya nyama zimenezi siikanatha kuchotsa machimo athu koma inali kungoloza kwa Mpulumutsi wathu Yahusha amene analowa m’malo mwa machimo athu. Unsembe wa Alevi ndi Unsembe wa Melkitzadeq. Yahusha tsopano ndi Mkulu Wansembe wathu ndi Mfumu ya chilungamo chotero miyambo ya mkachisi, unsembe wa Alevi ndi nsembe za

nyama sizikufunikanso. Komabe, sitingalakwitse zimenezi chifukwa chonyalanyaza masiku aphwando a pachaka a Yahuwah amene ali amuyaya, kuti atiphunzitse dongosolo lake lodabwitsa la chiombolo. Palibe kusiyana m'Malemba pakati paMadyerero a Chaka ndi Chaka ndi Madyerero a M'sabata monga nthawi zonse zoikidwiratu zolambirira Yahuwah. Masabata opatulika amenewa ndi omangika kosatha. Kumvera kumakhazikitsa malamulo a Yahuwah onsewo. *Aroma 3:31.*

Malamulo ochokera kwa Yahuwah ukawamvera ndi kuwasunga amapereka moyo. MBONI za Yahuwah zili zotsimikidzika ndi kupatsa nzeru zopambana.Ndipo zosatira za kumvera YAHUWAH ndiwo madalitso onse amene ife timakumana nawo tsiku ndi tsiku monga kukondwa kwa moyo komanso mtendere wake umene YAHUSHA adatisiyira.

Maweruzo a Yahuwah ndioona ndi olungama onse. Zofunika koposa golidi, Inde kuposa golidi wabwino wochuluka. Komanso, mwa izo mtumiki wanu amachenjezedwa nazo ndipo ine mKudzisunga muli Mphoto Yaikulu." *Salmo 19:7* mpaka 11. Yahuwah adakambanso kuti:Ndidawapatsatso malemba anga ndi kuwadziwitsa maweruzo anga ndiwo munthu akawachita adzakhala nao ndi moyo.Tikawerenga pa Ezekiel 18:20 ndi Ezekiel

20:11.Yahuwah akulonjeza mdalitso chifukwa cha kumvera malamulo komanso nyengo zake zoikika monga masabata,misasa,pasaka ndi ena ambiri.Pakumvera nyengo izi YAHUWAH amatsindikidza chidzindikiro anthu ake onse okhulupirika. Ndipo YAHUWAH sasitha choncho malamulo,malemba ndi maweruzo ake sadzasitha kunthawi zonse.

Yahuwah akufuna anthu tonse amene tikuyembekedzera kudzanso kwachiwiri kwa mpulumutsi wathu Yahusha tikhale osunga mawu ake.

Tikawerenga pa yohane 15:14 komanso 14:15, Yahusha anati ngati tikonda iye tikuyenera kusunga komanso kumvera zomwe iye adatilamulira kuti tichite.

Nkhani yachipulumutso ndi kulandira madalitso kuchokera kwa YAHUWAH zimafuna kumvera kwathuthu.popanda kumvera palibenso madalitso ndi chipulumutso chanthu.

Ngati mukufuna kumva zambiri zokhuza maphunziro a ***KALENDALA YA PANGANO LA YAHUWAH***

tipezeni pa manambala awa:

***0888707002 /0999856135/ 0988327284***

Kapena:

https://malawioutreach.teachery.co/

studythecalender.com

SHALOM